Pemphero Lingakuthandizeni Kukhala pa Ubwenzi ndi Mulungu (Gawo 3)

Zoti muchitezi zachokera m'mutu 17 wa buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa webusaiti ya jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mofatsa zimene mumakhulupirira komanso chifukwa chake mumazikhulupirira, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, komanso onani mmene mungafotokozere kwa ena zomwe mumakhulupirirazo.

KODI MULUNGU AMAYANKHADI MAPEMPHERO ATHU?

1 GANIZIRANI MOFATSA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

N'chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti inde?

N'chifukwa chiyani anthu ena angayankhe kuti ayi?

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

N'chifukwa chiyani mumakhulupirira zimenezo?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Mulungu amayankha mapemphero athu m’njira zosiyanasiyana.
(Onani mutu 17 m’buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 16-18.)

Werengani Miyambo 12:25; Aheberi 1:13, 14; Yakobo 2:16.
Kodi Yehova angagwiritse ntchito bwanji angelo komanso Akhristu anzathu poyankha mapemphero athu?

Werengani 2 Akorinto 4:7.
Kodi Yehova angatipatse chiyani kuti tithe kulimbana ndi mavuto amene tikupempherera?

Bambo wanzeru amasankha nthawi yoyenera yopatsa ana ake zinthu zimene anawo akufuna. Mofanana ndi zimenezi, Yehova amasankha nthawi yabwino yoyankha mapemphero athu

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Tiyenera kulimbikira kupemphera, ndipo tizikhulupirira kuti Yehova atiyankha m’njira yabwino kwambiri.

(Onani mutu 17 m’buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 19-20.)

Werengani Luka 11:5-10.

N’chifukwa chiyani tiyenera kupitirizabe kupemphera ngakhale pamene zikuoneka kuti Yehova akuchedwa kuyankha?

Werengani Afilipi 4:13.

Ngati Yehova wasankha kuti asatithetsere vuto limene tikupempherera, kodi akhozanso kuyankha pemphero lathulo m’njira iti?

Kodi Yehova wayankha mapemphero **anu** m’njira ziti? Perekani zitsanzo.

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI…

Mulungu sasamala za anthufe choncho sangayankhe mapemphero athu.

MUNGANENE KUTI…

N’zomvetsa chisoni kuti anthu ambiri amaganiza choncho. Koma ndaona kuti mfundo iyi ndi yokhazika mtima pansi…

_____

_____

Kodi ndi lemba liti limene mungamuwerengere munthuyo?

_____

Poganizira zimene munthuyo wanena, kodi mungafotokoze bwanji lembalo?

_____

WINA AKANENA KUTI…

Mulungu ali ndi mphamvu kuposa munthu aliyense ndiye ayenera kumayankha mapemphero athu nthawi yomweyo.

MUNGANENE KUTI…

Anthu ambiri amaganizadi choncho, koma n’zothekanso kuti…

_____

_____

Kodi ndi lemba liti limene mungamuwerengere munthuyo?

_____

Poganizira zimene munthuyo wanena, kodi mungafotokoze bwanji lembalo?

_____

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania